

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitsa
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

WABODZawe, SAMALA!

*(Nkhaniyi yatengedwa kuchokera
pa Machitidwe 5:1-11)*

Tsiku la Pentekoste litangotha, ambiri mwa Akhristu amene anangotembenuka mtima kumene anagulitsa nyumba ndi minda yawo. Iwo adabweretsa ndalamazo kwa atumwiwo amene “anagawira yense monga kusowa kwake. (Machitidwe 4:35). Kwa nthawi yochepa, ojera mtimawa a ku Yerusalemu anagawana zinthu zonse mofanana, ndipo anali nkuyanjana tsiku ndi tsiku komanso kukhalabe m'chiphunzitso cha atumwi. Machitidwe oterewa sanachitike kwa nthawi yaitali ku Yerusalemu komanso Akhristu a ku madera ena sanazitsatire. Akhristu a ku Yerusalemu samachita kukakamizidwa kuti agulitse zinthu zawo zonse, koma kuti aliyense amachita mwaufulu ngati chizindikiro cha kugwirizana ndi kuyanjana kwao.

Tangoganizani chigulu cha Akhristu, osangalala m'chikhulupiriro chawo chatsopano, akubweretsa ndalama kwa atumwi zochokera ku katundu wao wosiyanasiyana wa zimene iwo agulitsa. Iwo anaika maganizo awo pa zinthu zakumwamba ndipo amachita kukhala ngati “akugulitsidwa zonse” pokonzekera kubweranso kwa Yesu Khristu. Pa nthawi iyi ya kupembedza kwapadera, bambo wina ndi mkazi wake otchedwa Hananiya ndi Safira naonso anagulitsanso munda wao. Komabe, mosiyana ndi ena, amene mwachimwemwe anagulitsa katundu wao napereka ndalama zonse ku mpingo, Hananiya ndi Safira atakambirana, anagwirizana zosungako zina mwa ndalamazo. Zinali ndalama zawo, ndipo samakamizika kuti apereke chilichonse; komabe iwo anagwirizana kuti poperekapo akanene ngati akupereka ndalama zonse zimene anazipeza.

Zikhoza kutheka ku polowa mnyumba ya mapemphero ija, Hananiya analowa akumwetulira pamene anayamba kuwauza ena za mmene anagulitsira munda wake ndipo anabwera kudzapereka ndalama zonse ku tchalitchi. Monyadira komanso modzionetsera ngati kuti ndi wodzichepetsa, iye anapereka ndalamazo kwa atumwi. Mtumwi Petro, poona zimene zimachitikazo, anamufunsa kuti, “Hananiya, Satana anadzaza mtima wako chifukwa ninji kudzanzyenga Mzimu Woyera, ndi kupatula pa mtengo wake wa mundawo? Pamene unali nao, sunali wako kodi? Ndipo pamene unagulitsa sunali m'manja mwako kodi? Bwanji chinalowa ichi mumtima mwako? Sunanyenga anthu, komatu Mulungu.”

Mwadzidzidzi, Hananiya anagwa pansi nafa. Tsikulo silinathe monga momwe Hananiya ankayembekezera; moyo wake wosatha unali utayamba, ndipo mumtima mwake munali uchimo ndi chinyengo. Hananiya sanafunikire kupereka kalikonse ku mpingo. Akanakhoza ngakhale kupereka limodzi ma magawo asanu nasungako zina zonsezo. Tchimo lake linali lakuti ananama. Iye ananena zabodza pofuna kuwanyenga ena kuganiza kuti iye akupereka zonse. Komabe, tchimo lalikulu, monga momwe Petro analifotokozerana, linali lakuti Hananiya ananamiza Mulungu mu mtima mwake. Pamaso pa Mulungu ndi anthu, tchimo lake la kunama komanso chinyengo linawululidwa ndipo poweruza, Mulungu anamupha Hananiya.

Mantha aakulu anadza pa aliyense amene anaona kapena kumva zimene zinachitikazo. Chiweruzo choopsa cha Mulungu pa tchimo la chinyengo ndi chinyengo chinawonekera kwa onse. Khamu la anthu litagwidwa ndi mantha ndipo amadzifufuza. Anyamata

(Yapitirira pa tsamba 2)



“Hananiya, Satana anadzaza mtima wako chifukwa ninji kudzanzyenga Mzimu Woyera? ...Sunanyenga anthu, koma Mulungu.”

Mau a Mkonzi

Kalozera wa Baibul

Lamulo la Kuona
Mtima

Funso Yanko

Kodi Mukudziwa?

Nthano Ya Khola La
Ng'ombe

3

4

5-6

7

Mau a Nyengo Yake

8

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

anakulunga mtembo wa Hananiya ndi kupita nawo kumanda tsiku lomwelo, malinga ndi mwambo wakale wa Ayuda.

Patatha maola atatu, Safira, osadziwa chimene chachitika, anafika pamalo pamene amapempherapo. Petro anayandikira kwa iye namufunsa kuti, “Undiuze, ngati wagulitsa mundawo pa mtengo wakuti?” Safira anavomera motsimikiza. Petro anayankha kuti, “unapangana pamodzi bwanji kuyesa Mzimu wa Ambuye?”



Ngati chiweruzo
cha Mulungu chitati
chiwagwere onse
abodza ndi achinyengo
m'mpingo ya lero
lino, kodi ndani
amene angaimebe?

Taona, mapazi ao a iwo amene anaika mwamuna wako ali pakhomo, ndipo adzakunyamula kutuluka nawe.”

Nthawi yomweyo, nayenso Safira anagwa pansi nafa. Anyamata omwe aja adalowa natenga mtembo wake ndi kukauika pambali pa mwamuna wake. Chiweruzo cha Mulungu chinalinso chimodzimidzi kwa Safira munga momwe zinalili kwa mwamuna wake. Naye anavomera kuchita nawo chinyengo ndipo chiweruzo cha Mulungu pa iye sichinasiyane ndi cha mwamuna wake.

Malemba amanenetsa mobwereza kuti mantha anafalikira pakati pa anthu chifukwa cha chimemechi. “Ndipo anadza mantha aakulu

pa Mpingo wonse, ndi pa onse akumva izi.” Mantha omwewo a Mulungu abwere pa anthu onse amene ali mumpingo ndi amene ali kunja kwa mpingo. Zoonadi, anthu anayamba kuunguza miyoyo yawo ndipo anali kuchita mantha pa kulankhula, kuchita, kapena kukhala mwachinyengo. Ngakhale kuti zinthu zikatere, mitima ya anthu imatengeka, nthawi zambiri sizitenga nthawi yaitali, ndipo kenaka anthuwo amabwereranso ku makhalidwe awo amasiku onse.

Ngati chiweruzo cha Mulungu chitati chiwagwere onse abodza ndi achinyengo m'mpingo ya lero lino, kodi ndani amene angaimebe? Ambiri amene amadzitcha Akhristu akukhala m'moyo wachinyengo ndipo sali oona mtima kwa Mulungu, iwo eni, kapena ena. Nzoona kuti Hananiya ndi Safira ayenera kuti anadzipereka ndithu, komabe nsembe yawowo sinapose chinyengo chawo. Chiphunzitso cholungama ndi ntchito zabwino siziyeretsa kapena kulungamitsa lilime lonama.

Pamapeto ake chiweruzo cha Mulungu chidzafika; imfa yamuyaya ikuyembekezera iwo amene ananena bodza ndipo sanalape machimo awo. Kodi mudzasiyidwa? Wabodzawe, Samala! ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulungiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Mutipempherere ife; pakuti takopeka mtima kuti tili nacho chikumbumtima chokoma m'zonse, pofuna kukhala nao makhalidwe abwino. —Ahebrei 13:18

Pemphero la mtumwi Paulo linali lakuti akhale ndi chikumbumtima chosatsutsika ndiponso kuti mu zonse akhale nawo m'moyo oona mtima. Ambuye apangitse kuti anthu onse amene ali ndi chikhumbo chofuna kumutumikira azindikire kufunikira kwa moyo wokhulupirika ndi woona mtima tsiku ndi tsiku. Taitanidwa kukhala moyo wachiyero ndi wopanda chinyengo.

Mutu wathu ulendo uno uli pa nkhani ya Kukhulupirika. Ngakhale zikuoneka zazing'ono, koma ndizofunika. Ndi zomvetsa chisoni kuti pali anthu ambiri amene amadzitcha Akhristu amene amabera, kuba, kunama, ndi kuchita chinyengo. Kusakhulupirika kuli ponseponse mu nkhani, mu ndale, mu zamasesero, mu mabizinesi ndi zina zotero. Kuphatikiza apo, katangale ndi amene waononga chikhalidwe cha anthu m'zinthu zambiri. Ngakhale kuti zoterezi zimayembekezedwa m'dziko lauchimo, siziyenera kuti zidzikhalapo pakati pa anthu a Mulungu. Kukhulupirika pa “zinthu zonse” ndi kofunika kwambiri kuti munthu akhale wotsatira wa Yesu Khristu.

Nkodabwitsa kuona mmene anthu angayesere kulungamitsa kapena kuvomereza kuti chinyengo ndi kusakhulupirika zichitike ngati ziwapindulire—kuyambira pa mau olankhulidwa kwa ana, ku kuchita zamalonda, kukambitsana kwa m'banja, kwa ana ndi makolo awo komanso kwa anthu okhometsa misonkho. Bodza limodzi lenilenili ndi lokwanira kuti munthu asakalowe Kumwamba. Sizitengera kuti munthu ali ndi chizolowezi chonama, pamangofunika bodza limodzi basi. Ndi kwabwino kuvomereza cholakwa, chofooka, kapena kusowekera nzeru, kusiyana ndi kunama pofuna kuthawa udindo. Zoonadi, ambiri a ife tinalonjezako chinachake ndipo taiwala. Ngakhale kuti limenelo si bodza, popeza sizinachitike mwadala, tiyenera kusamala ndi mau athu. Pamene Mwana wa Mulungu akuuzani kuti adzachita chinachake panthawi yakuti yakuti, muyenera kuyembekezera kuti zidzatero ndithu. Akhristu ambiri akukhala m'moyo wachisawawa komanso osasamala ndi mau awo, ndipo umenewu si umboni wabwino kudzikira lapansi.

Ndi dalitso kukhala m'moyo wokhulupirika. Ngakhale kuti timalakwitsa, pokhala anthu pena timalephera kukhala angwiwo, nkumaiwala zinthu nthawi zina, pamakhala mtendere waukulu m'moyo woona mtima. Owerenga aliyense alimbikitsidwe kuti apitirize kukhala m'moyo wokhulupirika ndi wangwiwo.

Michael W. Smith

January 2022



*Mukafuna kutipeza
pa intaneti, mulembe
www.thegospeltruth.org
kuti mudzilandira makalata
athu kapenanso kuti
muone makalata akale.*

NTHANO YA KHOLA LA NG'OMBE

Ndikudziwa mkulu wina amene amagwira ntchito kuti asamalire ana amasiye. Anawo amagona mu nyumba ina imene inali yakuda ndi fumbi ndipo amasowekera zinthu zambiri za moyo uno. Mumtima mwanga ndimafuna kuthandiza ana amasiyewo, komabe mwanzeru ndinafuna kudziwa kaye ngati munthu angakhale okhulupirika ndi zazing'ono. Tsiku lina ndinapeza ndalama ndipo ndinamugulira bamboyo ng'ombe yamkaka kuti anawo adzimwa mkaka. Ng'ombeyo imafunika khola kuti idzikhala yotetezeka ku dzuwa ndi mphopo. Choncho potsatira pempho la mkuluyo, ndinamusiyira

ndalama zambiri kuti athe kugula kapena kumanga khola labwino. Pamene ndinabwerera ulendo wachiwiri, ndinayang'ana kuti kholalo lilipati. Koma sindinalipeze.

Funso limene anthu ambiri amafunsa ndi ili lakuti “chifukwa chiyani simunandithandize?” Ndipo yankho lake ndi lakuti: “Kodi khola la ng'ombe lili kuti?”

Monga Yesu ananenera pa 16:10, “Iye amene akhulupirika m'chaching'onong'ono alinso wokhulupirika m'chachikulu; ndipo iye amene ali wosalungama m'chachikulu.”



Kalozera posanthula Baibulo

Mutu: Kuona mtima

Kuwerenga Malemba: *Milomo yonama inyansa Yehova; koma ochita ntheradi amsekeretsa.* —Miyambo 12:22

Tanthauzo: Kuona mtima kumatanthauza kukhala, “Wopanda chinyengo; wachoonadi ndi woona mtima...wolondola kapena wakhalidwe abwino” (*Oxford English Dictionary*). Kuona mtima ndi khalidwe lokhala wokhulupirika. “Kupewa kunama, chinyengo, kapena kuba” (*Collins English Dictionary*).

Mwachidule: Chikhalidwe cha Mulungu ndi choyera ndi choona; Iye amadana ndi kusaona mtima kwamtundu uliwonse. Akhristu ayenera kukhala oona mtima m’magawo onse a moyo—m’mau ndi m’kuchita. Kusaona mtima ndiko kuphwaya makhalidwe abwino ndipo kudzabweretsa chionongeko chosatha.

I. Mulungu wa choonadi

- A. Duteronomo 32:4 Mulungu wa choonadi.
- B. Ahebri 6:18 Nzosatheka kuti Mulungu aname.
- C. Tito 1:2 Mulungu sanganame.

II. Chiyambi cha kukhala oona mtima

- A. Yohane 8:44 Mdierekezi ndiye atate wa mabodza.
- B. Yeremiya 9:5-6 Anthu amaphunzitsa lilime lawo kunena bodza.

III. Mulungu amadana ndi kusaona mtima

- A. Miyambo 6:16-17 Ambuye amadana ndi lilime labodza.
- B. Masalmo 101:7 Sadzakhala mu nyumba ya Mulungu.
- C. Miyambo 21:3 Chilungamo ndi choposa nsembe.

IV. Kulamulidwa kuti tisaname

- A. Levitiko 19:11-13 Usabe, kunamizana kapena kunyenga.
- B. Akolose 3:9 Bodza ayi.

V. Mboni yabodza

- A. Eksodo 20:16 Usamnamizire mnzako.
- B. Miyambo 12:17 Kunena zoono mwachilungamo.

VI. Kunena zoono

- A. Masalmo 34:13 Milomo yanu isalankhule zonyansa.
- B. Aefeso 4:25 Tayani kunena bodza, lankhulani choona.

VII. Musalumbire, musalonjeze

- A. Mateyu 5:37 Kuvomera kwanu kudzikhala inde.
- B. Yakobo 5:12 Musalumbire.

VIII. Kuona mtima kwa Mulungu ndi iwe mwini

- A. Masalmo 15:1-3 Lankhula choona mu mtima mwake.
- B. 1 Yohane 1:6 Kunena zabodza ndiko kunama.
- C. Afilipi 4:8-9 Lingalirani pa zinthu zimene zili zolondola ndi zoono

IX. Malangizo a kukhala oona mtima

- A. 2 Akorinto 8:21 Kupereka zinthu zoono mtima.
- B. 2 Akorinto 4:2 Kukana kusaona mtima ndi ukapsali.
- C. Machitidwe 24:16 Khalani ndi chikumbumtima chopanda ochitsutsa.
- D. 1 Petro 2:21-22 Chitsanzo cha Khristu—opanda chinyengo.

X. Chofunikira mwa Atsogoleri

- A. Eksodo 18:21 Sankhani amuna a choonadi.
- B. Machitidwe 6:3 Sankhani amuna oona mtima.

XI. Kunyenga/Bizinesi/Misonkho

- A. Miyambo 11:1 Masikelo achinyengo amamunyansa.
- B. Yeremiya 22:13 Nyumba yomangidwa ndi chisalungamo.
- C. Ezekiele 22:13 Phindu lachinyengo.
- D. Aroma 13:7-8 Lipirani misonkho. Musakhale ndi ngongole ndi munthu.

XII. Mtengo wake wa kukhala oona mtima

- A. Miyambo 16:8 Kwabwino zochepe ndi chilungamo.
- B. 1 Petro 3:17 Kuzunzika chifukwa choona.
- C. Masalmo 15:4 Kulumbira ku kuvutika kwake.

XIII. Zolowa ndi madalitso

- A. Yohane 8:32 Choonadi chidzakumasulirani.
- B. Miyambo 12:19 Kukhazikika kwamuyaya.
- C. 1 Petro 3:10 Onani masiku obwino.
- D. Miyambo 16:13 Chosangalatsa cha mafumu.
- E. Masalmo 145:18 Ambuye ali pafupi.

XIV. Zotsatira za kusakhala oona mtima

- A. Luka 12:2 Zonse zidzaululika.
- B. Miyambo 19:5 Iye amene amalankhula bodza sadzapulumuka
- C. Chivumbulutso 21:8 Abodza onse gawo lawo ndi m’nyanja ya moto.

Kumaliza

Tiyendeyende koyenera, monga usana. — Aroma 13:13

Lamulo la Kuona Mtima

Dziko lathu likugwira ntchito molimba mokonzanso chabwino ndi choipa ndiponso kuchotsa muyezo uliwonse wa makhalidwe abwino monga momwe mlengi wa chilengedwe chonse walamula. Posawerengera za kufala kwa kusalungama ndi momwe timaonera nzeru zokhudza makhalidwe, Mulungu ali ndi lamulo la chikhalidwe limene dziko lidzaweruzidwe nalo.



Mulungu wa choonadi

Uchimo unafotokozedwa ndi kuvumbulitsidwa kudzera mu Chilamulo cha Mose komanso unalembedwa m'mitima ya anthu panthawi yachilengedwe, kotero kuti chikumbumtima chikachitira umboni za lamulo lachilengedwe la Mulungu. Kuona mtima ndi kunena zoonza n'zofunika kwambiri pa makhalidwe abwino amene Mulungu anakonza. Kusaona mtima kwa mtundu uliwonse (kunama, chinyengo, kuba) ndi kosemphana kwathunthu ndi dongosolo ndi zofunika za Mulungu pa moyo wachikhristu.

“Kunama—kunena mwadala zinthu zimene si zoonza ndi cholinga chonyenga—ndi chipatso cha uchimo.”

Mulungu ndi woyera, wangwirowo, oona mtima ndipo ali “Mulungu wokhulupirika ndi wopanda chisalungamo;” (Duteronomo 32:4). Iye ali “Mulungu wokhulupirika ndi wopanda chisalungamo” (Ahebri 6:18). Kusaona mtima kuli kosemphana ndi gwero lenileni la chikhalidwe chake, pakuti Iye ali wangwirowo ndiponso chitsanzo chenicheni cha choonadi.

Chiyambi cha Kusaona mtima

Kunama kunena mabodza ndi machitidwe amene amafalikira. Malinga ndi kunena kwa Khristu, Satana ndiye tate wa makhalidwe oipa ndi kuonongeka kumeneku. “Inu muli ochokera mwa atate wanu mdierekezi...pakuti mwa iye mulibe...pakuti ali wabodza, ndi atate wake wabodza” (Yohane 8:44). Kunama ndi kusaona mtima konse ndi kwa mdierekezi. Yeremiya 9:5-6 imakamba za amene anapatuka kwa Mulungu, nanyenga anansi awo, ndi kuti “aphunzitsa lilime lao kunena zonama.” Ndi mtima wodetsedwa ndi mphamvu ya thupi motsogozedwa ndi Satana zimene zimachititsa munthu kunena bodza.

Malamulo otsutsana ndi kunama

Lilime lonama ndilo chimodzi mwa zokwana 6 zimene Mulungu amadana nazo monga zanenedwa pa Miyambo 6:16. Palibe chifukwa chokwanira chakuti Mkhristu anenere bodza, ngakhale kuti

ndi laling'ono bwanji. “Wakuchita chinyengo sadzakhala m'kati mwa nyumba yanga; wakunena mabodza sadzakhazikika pamaso panga” (Masalmo 101:7). Palibe mlingo wa kuzindikira zaumulungu, chiyezo cha chiphunzitsa, kapena ntchito zabwino zomwe zidzakanize moyo wa kusaona mtima, popeza “Kuchita chilungamo... kupambana ndi nsembe kumkonda Yehova” (Miyambo 21:3).

Malamulo a mu Chipangano Chakale ndi omveka bwino: “Musamaba, kapena kunyenga, kapena kunamizana....Usamasautsa mnansi wako, kapena kulanda zake” (Levitiko 19:11-13). Chimodzimodzinso, “musamanamizana wina ndi mnzake; popeza mudavula munthu wakale pamodzi ndi ntchito zake” (Akolose 3:9). Kunama—kunena mwadala zinthu zimene si zoonza ndi cholinga chonyenga—ndi chipatso cha uchimo. Mwana wa Mulungu sakuyeneranso kuyenda kapena kulankhula ndi mtima kapena lilime lonyenga.

Nenani choonadi

Limodzi mwa Malamulo Khumi ndilo, “Usamnamizire mnzako” (Eksodo 20:16). Kunena zinthu zabodza zokhudza munthu wina ndiko kuphwanya lamulo la Mulungu. Kumeneko ndi kuswa makhalidwe abwino. Zochita ndi zolankhula za Mkhristu ziyenera kukhala zangwirowo ndi zoonza mtima. “Uletse lilime lako lisatchule zoipa, ndipo milomo yako isalankhule chinyengo” (Masalmo 34:13). Paulo anawauza Aefeso kuti achotse zonyansa ndi kunena zoonza (Aefeso 4:25).

Osalumbira, Osalonjeza

Anthu ambiri amagwiritsa ntchito mau akuti, “Ndikulumbira kuti...” kapena “Ndikulonjeza kuti....” Ngati Akhristu salumbira kapena kulonjeza, kodi zikutanthauza kuti iwo sali oona mtima kapena kuti zimene akunena sizingakhale zoonza? Malemba amalangiza oyera mtima kuti “musalumbire, pemphelo kutchula chifundo...koma inde wanu akhale inde, ndi iai wanu akhale iai” (Yakobo 5:12). Yesu anaphunzitsa anthu kuti “koma manenedwe anu akhale, Inde, inde; Iai, iai; ndipo choonjezedwa pa izo chichokera kwa woipayo” Mateyu 5:37. Kunenanso kwina, Mkhristu safunikira ndipo sayenera kulumbira kapena kulonjeza kanthu. Ngati Mkhristu anena chinachake, chikuyenera kukhala choona, choona mtima, ndi chopanda chinyengo.

(Yapitirira pa tsamba 6)

Kulonjeza kumachepetsa choonadi cha zinthu zomwe zimanenedwa koma sizinalonjezedwe.

Mkhristu ali ndi udindo wochita zinthu moona mtima ndi aliyense, mosasamala kanthu za msinkhu kapena udindo. “pakuti tikonzere pambuyo, sipamaso pa Ambuye pokha, pambuyo pa anthu” (2 Mbiri 8:21). Paulo analankhula za oyera mtima mu 2 Akorinto 4 kuti “koma takaniza zobisika zachinsinsi, osamva mochenjerera, kuchita nao mau a Mulungu kunyenga.” Si zochita ndi mawu chabe koma cholinga chenicheni ndi cholinga chimene chiyenera kukhala chowonadi. Khristu anatisiyira chitsanzo chimene tiyenera kutsatira. Mkamwa mwake munalibe chinyengo kapena chinyengo (1 Petro 2:21-22). Anali



woona mtima, woona, ndi woona mtima. Mkhristu aliyense ayenera kuchita zinthu ngati mmene Paulo anachitira, kuti akhale ndi “chikumbumtima chosanditsutsa cha Mulungu ndi anthu” (Machitidwe 24:16).

Kuona mtima pamaso pa Mulungu ndi kwa iwe mwini

“Kuona mtima kwa iwe mwini ndi kwa Mulungu ndiyo njira yokhayo ya kukula mu uzimu ndi kukhala okonzekera chiweruzo.”

M’pofunikanso kwambiri kukhala oona mtima pamaso pa Mulungu ndiponso kwa munthu wekha. Davide anafunsa Mulungu kuti, “Yehova, ndani adzagonera m’chihema

mwanu?” Limodzi mwa mayankho anali akuti Iye amene “anena kuonadi mwake mwake” (Masalmo 15:1-3). Anthu ena amadzinamiza kwambiri mwakuti amayamba kukhulupirira mabodza awo omwe ndipo amakhala mu zinthu zenizeni. Sizabwino ndiponso ndi zolakwika. Mkhristu ayenera kulingalira ndi kuganiza pa zinthu zimene zili zenizeni, zoon, ndi za mbiri yabwino (Afilipi 4:8-9). Kuwonjeza apo, pa 1 Yohane 1:6 amati, “Tikati kuti tiyanjana ndi Iye, ndipo tiyenda mumdima, tinama, ndipo sitichita choonadi.” Mulungu amadana ndi chinyengo chamtundu uliwonse, ndipo aliyense ayenera kukhala woona mtima mu nzeru ndi mu uzimu. Kuona mtima kwa iwe mwini ndi kwa Mulungu ndiyo njira yokhayo ya kukula mu uzimu ndi kukhala okonzekera chiweruzo.

Kukhulupirika mwa atsogoleri

Popeza kukhulupirika nkofunika kwa Mkhristu, ichi ndi chinthu chenicheni chowayenereza iwo amene ali atsogoleri mu mpingo. Atsogoleri osankhidwa a Israele anayenera kukhala “amuna a choonadi” (Eksodo 18:21), ndipo atumiki amene anasankhidwa pa Machitidwe 6:3 anayenera kukhala “amuna a mbiri yabwino.”

Chinyengo/Bizinesi/Misonkho

Akhristu ayenera kukhala oona mtima mu zinthu zonse; ndipo zimenezi zikuphatikizapo kunyumba,

kusukulu, kuntchito, mu zamalonda, ndi za boma, ndi zina zotero. Chinyengo ndi pamene kuba ndi kunama zimakumana pamodzi. Yereimiya analankhula za wina amene anamanga nyumba yake mwa njira zosalungama ndipo sanawalipire amisiri amene amawagwirira ntchito (Yereimiya 22:13). “Muyeso wonyenga unyansa Yehova; koma mulingo wamphumphu umsekeretsa” (Miyambo 11:1). Akhristu enieni adzabweza ngongole zao, amagwira ntchito zaozao, adzakhala oona mtima m’zamalonda zirizonse, ndipo sadzabera mwadala munthu aliyense kapena pang’ono. Pokhala moyo woona mtima, oyera mtima adzapereka mndandanda wa mmene wapereka misonkho ku boma pa nthawi yake (Aroma 13:7-8). Pamene Akhristu anena chinachake, chimene chikhoza kukhala choona ndi cholondola, ndipo zochita zawo ziyenera kutsatiridwa. Chilichonse chimene chapangidwa osawerengera kuona mtima uchimo.

Mtengo wake wa kuona mtima

Padzakhala nyengo zimene tidzaononge nthawi ndi ndalama kuti tikhalebe oona mtima, koma izi ndi zokondweretsa kwa Mulungu. Salimo 15:4 limanena za iye amene: “Atalumbira kwa tsoka lake, sasintha ai.” Pamene wanena kuti uchita chinachake, ngakhale chitakhala chopweteka, chimenecho chitsatireni. Dziko limasintha ndi kubwerera mmbuyo, koma mwana wa Mulungu amayenda mwangwiro. Ndi bwino kukhala ndi zochepa ndi chilungamo (Miyambo 16:8) ndipo ndi kukhala ndi madalitso a Mulungu.

Mphoto ya kuona mtima

Kuona mtima ndi kunena zoon zimapereka ufulu popeza “choonadi chidzakumasulani” (Yohane 8:32). Mabodza amabwera ndikuchoka koma choonadi chimakhazikika (Miyambo 12:19), ndipo oona mtima sakuyenera kuopa kugwidwa mu bodza. Iwo amene amalankhula choona amalemekezedwa ndi kupatsidwa ulemu (Miyambo 16:13). Nyengo zokoma zimafika kwa iwo amene amalankhula mopanda bodza ndi chinyengo (1 Petro 3:10). Chofunika kwambiri, “Yehova ali pafupi ndi onse akuitanira kwa Iye... akuitanira kwa Iye m’choonadi” (Masalmo 145:18).

Zotsatira za kusaona mtima

Palibe chimene chimachitika kapena chonenedwa m’moyo uno chimene chidzakhala chobisidwa, ngakhale anthu akhala kuti anyengedwa kwa kanthawi. Zinthu zonse zidzavumbulutsidwa (Luka 12:2), ndipo palibe mboni yonyenga kapena wabodza amene adzapulumuka ku chiweruzo cha Mulungu (Miyambo 19:5). Kuona mtima si chinthu chakuti mwana wa Mulungu akhoza kusankha, ndi choyenera kuchitika ndithu. Amene akunena zabodza adzalandira chilango chofanana ndi iwo osakhulupirira ndiponso akupha popeza “onse a mabodza, cholandira chao chidzakhala m’nyanja zotentha ndi moto ndi sulufure” (Chivumbulutso 21:8).

Tiyeni tikhale, tiganize, tilankhule, ndi kuchita zinthu moona mtima monga mmene Mau a Mulungu amatilamulira, popanda kunama, chinyengo, kapena kusaona mtima kwa mtundu uliwonse. ■



"Baibulo siligwirizana ndi chiphunzitso chakuti anthu amaona kuti zinthu sizingayende bwino. Choonadi cha Mulungu ndi chenicheni, ndipo bodza limasonyeza khalidwe lolakwika ndi chikhalidwe chake."

Kodi nkololedwa kunama kuti upeze china chabwino?

Malingana ndi kuona kwa dziko, mwina pali zochitika zina zimene zingaoneke zomveka kunama. Komabe, Baibulo limanena momveka bwino. 1 Petro 3:10 akutiphunzitsa mosapsatira kuti milomo yathu isalankhule chinyengo. Zimenezi zikutanthauza kuti chilichonse chimene tikunena chikuyenera kukhala choona, ndipo tiyenera kupewa miseche, mabodza, kunama ndi chinyengo. Lamulo limeneli silinali lodalira pa zochitika.

Baibulo siligwirizana ndi chiphunzitso chakuti anthu amaona kuti zinthu sizingayende bwino. Choonadi cha Mulungu ndi chenicheni, ndipo bodza limasonyeza khalidwe lolakwika ndi chikhalidwe chake. Mwana wanga wamkazi anandifunsa ngati ndinganame nditakhala kuti ndikuzembetsa Mabaibulo kuwalowetsa m'dziko limene amawaletsa. Ndikhoza kuswa lamulo la anthu kuti ndimvere lamulo la Mulungu popereka Mabaibulo. Sindikanadzipereka kuti ndichite zomwe ndinali kuchita; komabe, kutakhala kuti ndakumana ndi olamulira ndipo akundifunsa, sindikanatha kukana choonadi, ngakhale zitakhala kuti zikhoza kunditengera kundende.

Kunama ndi kunyenga ndiko kuphwanya zonse zabwino ndi zolondola. Pakali pano, zikhoza kuoneka kuti kunama kungathandize kwambiri, koma nkupita kwa nthawi kukhoza kubweretsa chiongeko. Chimodzi mwa kukongola kwa chipulumutso m'moyo ndi chiyero chomwe kumabweretsa-chimodzimodzi m'moyo wonse. Sakanizani bodza ndi choona, ndipo mudzapeza chinachake chodetsedwa chimene sichikhalanso choyera.

Kodi mungapereke malangizo otani kwa makolo pankhani ya kuona mtima?

Choyamba, makolo ayenera kukhala oona mtima nthawi zonse ndi ana awo. Ngakhale kuti si chanzeru kuti kholo lidziulula chilichonse chimeneyo mwana angafune kudziwa, kunama kumaononga kwambiri. Makolo ena amalondeje ana awo koma samakwaniritsa zimene alondeje. Izi zimaphunzitsa mwana kuti ndi bwino kunena chinachake panthawiyo ndipo alibe udindo wochichita. Ngati kholo liuza mwana

kuti adzapita kwinkwake kapena kuchita chinachake, ayenera kuonetsetsa kuti akusunga lonjezolo. Ana amaphunzira zambiri mwa kuyang'anitsitsa komanso zomwe akumana nazo kusiyana ndi zomwe timawauza pakamwa.

Chachiwiri, makolo ayenera kuphunzitsa ana awo kufunika kokhala oona mtima adakali aang'ono. Ali ndi zaka ziwiri kapena zitatatu, ana amaphunzira kunama, nthawi zambiri mwa kukana khalidwe loipa. Akafika zaka zinayi, ana amadziwa bwino kusiyana pakati pa choonadi ndi kunama ndipo nthawi zambiri amafuna kubisa cholakwacho. Kunama kumatha kukula mwana akamakula ngati sakusamala. Kafukufuku wina anasonyeza kuti ana 96 pa 100 alionse ananamako nthawi ina. Ambiri a iwo amanama kangapo patsiku.

Ndi bwino kuti makolo aziphunzitsa ana awo moona mtima komanso kuti azichita zinthu mwachilungamo. Mwana wamng'ono akanama, sizabwino. Amafunika kulangidwa ndipo khalidwe lawo liyenera kuwongoledwa mwamsanga ndi zotulukapo zoipa ndi zabwino zonse koterokuti aphunzire phindu ndi kufunika kwa kuona mtima.

Wina anandifunsa funso ndipo nthawi yomweyo ndinawauza zomwe sizinali zoono. Kodi ndachimwa?

Kusakhulupirika kwenikweni ndi pamene chinthu chanenedwa mwadala ndi cholinga chofuna kunamiza munthu. Ngati simunakonzekere, ndipo chinthu choyamba chimene chinatuluka kuchokera pakamwa panu chinali chongofuna 'kudziteteza' ndipo kenako munazindikira, limenelo si tchimo. Komabe, ndipofunika kuti mubwerere kwa munthuyo ndi kukakonza zimene mwanenazo, ngakhale zioneke kuti ndi zochititsa manyazi. Pali maphunziro oti muphunzire ndipo pali chenjezo pamene mukuyenera kubwerera ndikukakonza zinthu motero. Munthu akamalankhula chinyengo atachita kukonzekera, kumakhala kovuta kuti abweze zimene ananenazo, chifukwa mtima ndi wonyenga. Zikatero, pakufunikanso kuti alape, apo ayi sangapulumutsidwe.



KODI MUKUDZIWA?

76% ya anthu amakhulupirira kuti kunama ndikovomerezeka nthawi zina.
 24.1% ya amuna adanamapo za mbiri yawo ya Facebook pamene 16.6% ya akazi adateronso.
 21.7% ya amuna adanamapo za maphunziro ndi ntchito yawo pamene 16.3% ya amayi adateronso.
 51.7% ya amayi adanamapo za kulemera kwawo pamene 28% ya amuna adateronso.
 3% (mwa anthu 1,254 aku America omwe adafunsidwa) adanena kuti amanama kawirikawiri.
 66% ananena kuti samakhulupirika nkomwe kapena mwina mwapatapatali.
 Akazi amakonda kunamiza makolo awo ndipo amuna amakonda kunamiza anzawo.
(Kafukufuku waku America wa 2014 wopangidwa ndi CreditDonkey.com)



MBIYA YOPANDA KANTHU

(Kunena mwachidule nthano yaku China yakalekale. Analemba anali Demi.)

Pali nkhani ina imene imakambidwa ku China ya mnyamata wina dzina lake Ping. Iye anakonda maluwa ndipo chilichonse chimene anakdzala ndi kulima nthawi zonse chimaphukira ndi kukhala duwa lokongola. Mu ufumu umene Ping anakhala, mfumuyo inalibe mwana wamwamuna, koma inkafunika munthu wodzalowa m'malo mwake. Mfumuyo, yomwe nayonso inkakonda kulima, inagawa mbewu zamaluwa kwa anyamata a mu ufumu wonsewo. Aliyense amene akadalima duwa lokongola kwambiri kuchokera ku mbewu zake zija akanadzakhala mfumu mmalo mwake. Ping anabzala mosamalitsa mu mbiya yadothi mbewu ija analandira kuchokera kwa mfumu. Anayithirira ndi kuyisamalira mbewu ija, koma palibe chimene chinachitika.



Anyamata ena anabzala mbewu zao ndipo anali ndi maluwa ophuka m'mbiya zao. Iwo anaseka ndimukunyoza Ping yemwe anali adakali ndi mbiya yopanda kanthu. Ping anasintha nthaka n'kuikamo feteleza ndi nsomba zouma, koma sizinaphule kanthu. Pamapeto pake, tsiku linafika loti zomerazo zitengedwe kwa mfumu. Pakati pa chisangalalocho, Ping anali wokhumudwa, chifukwa anali adakali ndi mbiya yopanda kanthu. Bambo ake anamukumbutsa kuti anachita zonse zimene akanatha ndipo anafunika kukapereka kwa mfumu.

Ana a mu ufumuwo anafika kunyumba yachifumu ndi maluwa awo okongola. Mfumuyo inayang'ana zomera za anyamatawo ndi diso lakuthwa. Nkhope yake inachita tsinya kwambiri ataona mbiya ya Ping ili yopanda kanthu. Mfumuyo inafuula kuti, "Wandibweretsera mbiya yopanda kanthu!" Ping anadzutsa mutu wake nati, "Pepani, Mfumuyo. Ndinayesetsa kukulitsa mbewu imene munandipatsa, koma palibe chimene chinamera."

Mfumuyo inagwira chibwano chake ndi kumwetulira. Kenako inauza anthuwo kuti: "Mundilole kuti ndikusonyezeni mfumu yatsopano. Taonani, mbewuzo zinaphikidwa kuti zisakule. Sindikudziwa kuti nonsenu mbewu zanu munazikuliritsa motani, koma sizinamere kuchokera ku mbewu zanga. Uyuyu wakhala woona mtima komanso wachilungamo."

Phunziro ka nthanoli ndi lomveka bwino. Tikakhala okhulupirika, nthawi zina timakhala tokha pakati pa anthu amene atizungulira. Zikhoza kuoneka ngati kukhulupirikako kungabweretse mavuto, ndipo pena pakhoza kuoneka ngati pali njira ina yabwinoko. Komabe, mbiya yanu ikakhala yopanda kanthu, sunganibe ungwiro wanu, pakuti Atate athu akumwamba adzakupatsani mphoto pa nthawi yake. ■

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
 P. O. Box 2042
 Nixa, MO 65714
 USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

CHIYERO CHA KWA AMBUYE